Ndi _____

Kulingana ndi 10:25 a, ndi ciani cimene tisaleke kuchita?

ingo la likulu mu kusunkhana kwathu ndi ciani? Mu 10:25 b?

Ndiphindu yotani atipatsa mu 10:25 b mu Kusunkhana kawiri kawiri ndi a kristu anzathu?

Onani ndime zonse ziwiri, Aheberi 10:24 ndi 25 ziti phuzitsa kuti kusunkhana ndi anzathu kuli ndi phindu kwa iwo ndi ife. Tisamaganiza zimene tingathengemo mu kusunkhana ndi anzathu, koma tipezenso njira zodalitsa amene tisonkhana nao. Mau onena kuti “Wina ndi mzace” apezeka kwambiri mu cipangano catsopano. Onani aya mau a “Wina ndi mzace” mu Buku lopatulika. Lembani njira zina tinga tumikiremo ku anzathu.

Aroma 15:7 _____

Aroma 14:9 _____

1 Petro 1:22 _____

1 Petro 5:5 _____

Yakobo 5:16 (1) _____

(2) _____

Aefeso 4:1 ndi 2 _____

Aefeso 4:32 _____

Werengani Aefeso 4:1-16. Lembani zinthu zisanu ndi ziwiri ziri mu ndime 4-6 zimene zibweretsa mugwirizano pa a kristu onse. (Zonse ziyamba ndi mau akuti umodzi).

Ndime ya 11 inena pa utsogoleri usanu wosiyana mu utumki wamene Yesu apatsa kacisi yace. Ndiwotani?

Kulingana ndi ndime ya 12 utsogoleri uyu ugwira nchito yotani mu kacisi?

Pamene tilandila utumiki wace ndi zinthu zotani zimene zibwera mu umoyo wathu, kulingana ndi 4:12-16?



COCITA

Buku lopatulika limaitana kacisi thupi la kristu. Silinena kuti kacisi ili monga thupi, koma kuti kacisi ndi thupi la kristu. Kuli zinthu ziwiri zimene zilengesa ma thupi athu kugwirizana, zimene zionetsanso kugwirizana kwa thupi la kristu – kacisi. Coyamba mwazi umodzi upeleka cakudya ku ziwalo zonse. Mwazi wo peleka umoyo ngati weleka kufika ku ciwalo cili conse, cija ciwalo ciza mwalira. Motero munthu ali ciwalo ca kristu, ayeretsedwa ndi mwazi wa kristu. Kaciwiri umoyo wa munthu upezeka mu ziwalo zonse zathupi lace sumakhala cabe mu ciwalo cimodzi. Motero mzimu wa kristu ukhala mu ziwalo zonse za thupi lace.

Nthawi zonse ziwani kuti ndinu olumikizana ndi abale anu mwa kristu kupyolela mwa mwanzi wa Yesu ndi mzimu wa Mulungu. Ku gwirizana kwa thupi la kristu sicofunitsa koma ndi waYesu ndi mzimu wa Mulungu. Ku gwirizana kwa thupi la kristu sicofunitsitsa koma ndi coonadi.

Kulingana ndi Aefeso 4:3 tinga samale motani cigwirizano cathu?

PHUNZIRO 7: KUUZAKO ENA ZA CIKHULUPIRIRO CAKO

Pa mtsinje wa misisipi ku dziko la United States of America kulimangalawa ambiri amene amatenga anthu okonda kuyenda pa madzi. Oyendetsa ngalawa anali nayo nkhani yo uza anali mu ngalawa. Anawauza za ngalawa yace mwamene ina citira ngozi ndi ngalawa ina na mutaira mu madzi. Anali mu ngozi yayikuru yo mbira mu madzi, koma oyendetsa ngalawa ina anabwera na mupulumutsa.

Anati uja ndiye munthu anandipulumutsa. Kucokera tsiku ija ndimafuna kudziwitsa anthu ambiri za munthu uja ' ndili ndi umoyo cifukwa ca iye.'

Munjira yo lingana munthu ngati a pulumutsidwa ku cilango ca muyayaya mu nganjo la moto kupyolera mu cikhulupiliro mwa kristu, amafuna kuonetsa anzace wamene amu pulumutsa. Ndico funikira kuti a kristu auzeko anzao za Yesu kristu ndi cipulumutso cace.

Tikauzako anzathu zimene Yesu a ticitira mu umoyo wathu, ticitira zinthu ziwiri.

- ✓ Tiphereka ulemeloro kwa ambuye pa nchito yace yo tipulumutsa.
- ✓ Tipatsa ena m'pata wo dziwa za cikondi camulungu ndi ci pulumutso cace kwa iwo.



Lingo la phunzilori ndi kuthandiza kuuzako ena cikhulupiriro cako mwa kristu. Werengani macitidwe 1:8 Yesu ananena kuti ophunzira ace azakhala motani?

Mphamvu zocitira umboni azazicotsa kuti?

Yesu afuna tikhale mboni zace. Kukhala mboni kufunika zinthu zitanu:

- Mboni iyenera kudziwa coonadi
- Mboni iyenera ku konzekera ku patsa umboni.
- Mboni iyenera ku kunzekera kulangidwa cifukwa co perekera umboni. (Mau a witness ana cokera ku mau a cihelene onena kuti “Martus” amene a tanthauza kuti munthu wamene afera pa umboni wace.)

Tiyeni tione paizi zinthu zitanu

Coonadi.

Ndi cofunikira ku kwanitsa ku gawana coonadi ca uthenga wa bwino ku cokera mu cipangano catsopano. Mu buku la Aroma muli mundandanda wo sabvuta wo tumikiramo uthenga wa bwino kupyolera mu ndime zinai. Cimene muyenekera kucita ndi ku kumbukira ndime yo yamba, iyi ndi Aroma 3:23. Kumbali kwa iyi ndime mu buku lo patulika lanu lembani ndime yo tsatirapo ndi yo tsatiraponso paka mwalemba ndime zonse zinai.

Mundandanda wa mu Aroma

Aroma 3:23 itiuza mkhalidwe wa ku mzimu wa munthu ali yense. Ndiwotani?

(Kumbali ya Aroma 3:23 mu buku lopatulika lanu lembani Aroma 6:23 a)

Aroma 6:23a itiuza cocoka mu ucimo. Ndi ciani?

(Kumbali ya Aroma 6:32a mu Buku lopatulika lanu lembani Aroma 5:8) Aroma

5:8 itiuza cimene Mulungu anacita pamacimo athu. Ndi ciani

ici?

(Kumbali ya Aroma 5:8 mu Buku lopatulika lanu lembani Aroma 10:13)

Aroma 10:13 itiuza mwamene tinga landilire cipulumutso ca Mulungu. Ndi motani?

Umboni

Monga a kristu tinga peleke umboni wa uthenga wa bwino cifukwa tidziwa kuti ama pulumutsa amuna ndi akazi ku macimo ao ndi ku wapatsa umoyo osatha. Kodi tidziwa bwanji? Cifukwa ati pulumutsa! Tilinao umboni wa mphamvu wacipulumutso cace. Tinga peleke umboni wathu i.e kuuzako ena zimene za ticitikira. Mu phunziro loyamba tinaona kuti pali ma gawo atatu pa umboni uli onse. Ndiotani

1. _____

2. _____

3. _____

Kulingana ndi 1 Petro 3:15 ndi ciani cimene tiyenera kukhala okonzekera kucita nthawi zonse?

Pamene uphunzirira kugawanitsa umboni wako uzakhala nayo njira ya mphamvu yo citira umboni Yesu. Kulibe anagakutsutse pa zimene unapitamo mu cipulusto cako.

Mudyerekezi samafuna ngati tipereka umboni wa cipulumutso cathu. Mwaici amayesa kutiletsa kupereka umboni wathu. Amacita ici kupyolera mu kutiuza kuti umoyo wathu sulii bwino. Ndipo tilibe m'pata wo lankhula pa umoyo wathu, wa ci kristu. Kumbukirani, umboni wathu si wa zimene ta citira Ambuye, koma ndi wa zimene Ambuye aticitira! Ndico cifukwa cace tizakhala nawo umboni wo uzako anzathu nthawi zonse.

Mtengo wace

Sionse amene tiuza za uthenga wa bwino a zaulandira mo kondwera. Tinga kumane nazo zo titsutsa nthawi ndinthawi. Ici ndiye cinthu cina cimene satana anga sebenzetse kutiletsa kupereka umboni. Kulingana ndi cibvumbulutso 12:11,

ni zinthu zotani zitatu zofunika mu kungonjetsa mudani?

1. _____
2. _____
3. _____



ZOCITA

Pa onse opulumutsidwa, ambiri abwera kwa kristu kupyolera mwa iwo amene awadziwa, monga acibululu, abale, abwenzi, amene agwira nao nchito etc.

Kuzanja la manzere la malo ali panso lembani mazina a anthu osa pulumutsidwa amene mudziwa.

Kumbali kwa mazina aya lembani cifukwa cimene sana pulumutsidwe, monga, 'sana mverepe uthenga wa bwino,' 'Kuganiza kuti kulibe Mulungu,' kunkhala ndi cikulupiriro cina cace.' 'Kuonongeka,' kukonda Cuma etc.

- ✓ Pemphani Ambuye akupaseni m'pata wo pereka umboni kwa awa anthu.
- ✓ Pempherani kuononga zinthu zimene zicingiliza cipulumutso cao
- ✓ Pempherani kuti a kristu ena aza tumikira kwa iwo, ku simikiza umboni wanu.

PHUNZIRO 8 UBATIZO WA MADZI


M'busa anali kufotokoza zaubatizo kuli a kristu atsopano. Pamene anali kunena anali ku gwiritsa nchito ziwalo za manja ace. Kusewenzetsa dinso lace anaona cinthunzi ca zanja lace kumbali kwace. “kodi mwaciona cinthunzi ca zanja langa?” anafunsa. Cinthunzi si zanja langa, koma ciimilila zanja langa” ananena. “Motero pamene muna pulumusidwa ndipo ubtizo wa zoona unacitika.”

Muna batizidwa mwa kristu pamene muna khulupilira muna gwirizana ku mzimu ndi yesu kristu. Anakhala ndiye umoyo wanu. Anafa, anaikidwa mu manda, ndi kuuka kwa kufa, ndipo pamene muna khulupilira mwa iye zonse izi zinakucitikirani. Pamene mu batizidwa mu madzi ici ndi cinthunzi thunzi ca zinthu zimene zacitika kale mu umoyo wanu.”

Ubatizo ndi kulangiza cinthu cimene cacitika kale mu umoyo wa m'kristu. Ndi cidziwitso ca kunja cimene cisonyeza coonadi cili mkati. Ndi cintu coonetsa cimene cacitika mwa iwo ali mwa kristu.

Awiri ngati a kwatilana amapatsana mphete kulangiza cikwati cao. Munjira imodzi, ubatizo umalangiza cipulumutso. Kuvara mphete ya cikwati sici matipangisa kukhala okwatila kale, cimodzi modzi ubatizo wa madzi siutipulumutsa. Zonse ndi zizindikilo za kunja zimene zicitila umboni cimene ca citika kale.

Coonadi cakuti ubatizo ndi cidziwitso ca cipulumutso, osati cipulumutso ceni ceni, si cicepesa ubatizo. Munthu okkwatira ngati savara mphete ya cikwati anthu azaganiza kuti siwokwatira. Mu kusavara mphete uyu munthu asankha kusadziwika kuti ndiwokwatira. Munjira imodzi yo lingana ubatizo ndiye njira imene munthu amaoneseramo ubale ndi ambuye Yesu kristu mu cipangano catsopano.



Mu phunzitori tizaona kuti ubatizo ndi ciani.

Tizaona cimene Buku lopatulika li phunzitsa pa ubatizo wamadzi mu mitu itatu.

- ✓ Ndani ayenera kubatizika?
- ✓ Tiyenera kubatizika bwanj?
- ✓ Cifukwa ciani tiyenera kubatizika?

Ndani ayenera kubatizika?

Mukuyamba ca m'ma 200AD msogoleli wina wa mu kacisi woyamba ana phunzitsa makolo a cikristu kubwera ana ang'ono kuti awa batize. Msogoleli wina wo cedwa Tertullian anatsutsa ku phunzitsa kwatero cifukwa cikocikali cinaikidwa kutsogolo ya kavalo. Ubatizo kuligana ndi Buku lopatulika umatsatila

cikhulupiliro osati kuyambilira ai. Koma kubatiza ana ang'ono kunapitilila mu kacisi ndi kukhala mwambo m'ma 400AD.

Kucokera mu ndime izi lembani ngati ubatizo una yambilira kapena unabwera pa mbuyo ya cikhulupiliro.

Marko 16:16 _____

Macitidwe 2:38-41 _____

Macitidwe 16:14 ndi 15 _____

Macitidwe 16:31-34 _____

Ubatizo wamene cipangano ca tsopano cidziwa ndi wa munthu amene akhulupilira. Munthu ngati alandila Yesu kristu kukhala mpulumutsi wace ayenera kubatizidwa. Mu Buku lopatulika tiona kuti ubatizo umabwela ngati munthu akhulupilira mwa kristu osati pamene akalibe ku khulupilira.

Tiyenera kubatizika motani

Kodi tingabatizike moti wala waza madzi, kapena ku mbizidwa mu madzi? Kapena cilibe ncito? Mau a kuti “Baptize” acokera ku mau aciheleme akuti “Baptizo” katanthauza kuti ku mbiza mu madzi. Mau amenawa Amaya sebenzetsa paku sintha mtundu wa salu. Munthu ngati a pempha ku sintha mthundu wa salu yace, saza kondwela ku mubwezera yo wala waza. Kubatiza ku tanthauza ku mbiza cinthu conse mumadzi. Mu Buku lopatulika mupezeka batizo limodzi cabe, ili ndi lo mbiza mu madzi.

Kucokera mu ndime izi lembani ngati muganiza kuti anawa batiza kuwala waza madzi kapena ku mbiza mu madzi:

Mateya 3:16 _____

Macitidwe 8:36-39 _____

Yohane 3:23 _____

Cifukwa ciani tiyenera ku batizidwa

Ubatizo ucitira umboni kwa anthu ambiri zimene za citika mu umoyo wa mkristu. Ubatizo siuti pulumutsa. Tipulumutsidwa ndi cikhulupiliro mwa kristu. Pamene tinapulumsidwa tina batizidwa mwa kristu.

Werengani Aroma 6:3 ndi 4. Ndi zinthu zotani zitatu zinacitika kwa Yesu zimene zacitikanso kwa ife, pamene tina batizidwa mwa iye?

1. _____

2. _____

3. _____

Pamene anafa pa mtanda, tinafa naye pamodzi. Pamene anaikidwa mu manda, tinaikidwa naye pamodzi. Tigawananso umoyo wa kuukitsidwa kwace kupyolera mu ku batizidwa mwa iye.

Tipereka umboni kwa izi zoonadi za mu myoyo yathu pamene tibatizidwa mu madzi. Kumbiza mu madzi a ubatizo ndi kutulukamo ndi cithunzi thunzi ca imfa yathu, kuikidwa ndi kuukitsidwa ku umoyo wa tsopano mwa kristu.

Mwacidure

- ✓ Munthu ngati a pulumutsidwa ayenera kubatizidwa mosacedwa.
- ✓ Ana ang'ono ndi anthu amene sana khulupilire mwa Yesu kristu. Sayenera ku batizika. Ubatizo ndi wa iwo okhulupilira.
- ✓ Ubatizo umaonetsa anthu ambiri zimene zacitika mu umoyo wa okhulupilira. Umaonetsa kuti anafa na Yesu, kuikidwa naye ndi kuukitsidwa naye ku umoyo wa tsopano.
- ✓ Mwaici ubatizo siku wala waza madzi, koma kumbiza thupi lonse mu madzi.
- ✓ Cifukwa ubatizo wa madzi ndi kuonetsa anthu ambiri zimene zacitika mu myoyo yathu. Ndi cabwino kuitana acibale ndi a bwenzi, kweni kweni aja otsapulumsidwa kubwera kuubatizo wanu. Ndi m'pata wouza dziko kuti umoyo wanu wakale wafa, kuti mwaikidwa na yesu ndi kuuka ku umoyo wa tsopano mwa iye. Kulibe coposa ubatizo mu kuonetsa ici mwa mphamvu.



Zocita

Mukusiliza, kambilani pa izi

- Kodi una batizika?
- Kodi ulinayo mafunso pa ubatizo
- Ngati ukalibe ku batizika, kodi ungayankhe bwanji funso lili mu macitidwe 8:36?

PHUNZIRO 9 MZIMU WOYERA

Anthu awiri anayendela ku kaona Niagara falls, anagwidwa ndi mantha cifukwa ca maonekedwe a ici cilengedwe codabwisa. Kwa nthawi yaithali anaimilira pa mwamba pa uyu mpopoma wa madzi naona bwino. Onse awiri anakhala cete pamene anali kaona mpopoma wa madzi kupereka makumbi a mame kumwamba. Umodzi wa awiriawa wamene ana bweleko kale anati kwa mzace, “bwela kuno ndikuonetse cinthu cina.” Pamene anali kupita mu mbali ya Niagara falls ana pindamuka nauza mzace kuti “izi ndizo mphamvu zikuru kwambiri zimene sizima gwira nchito pano pa dziko.”

Mzace anaganiza pa nthawi ing'ono namuyankha; “kuchotsapo comodzi! Mzimu woyera ndiye mphamvu ikuru kwambiri imene siyi gwiritsidwa nchito!”

Yesu analonjeza ophunzira ace kuti aza kalandira mphamvu pamene mzimu woyera uzakabwela pa iwo. Mzimu woyera ndi munthu. Ndi Mulungu. Ndi umodzi wa mulungu patatu. Cipangano catsopano cinena panjira imene amabweleramo kwa okhulupirira onse, imene ubatizo wa mzimu woyera.

Buku lopatulika lifotokoza zolandira mzimu woyera munjira zambiri, monga , “kabatizika ndi mzimu woyera,” “kuzula ndi mzimu woyera,””mzimu oyer a unagwa pa iwo” “mpaso ya mzimu woyera inadza pa iwo,” “ndituma lonjezo la atate pa inu,” etc. mosakondweretsa a kristu ambiri mu myoyo zao amakhalila mwa mphamvu zao okha. Mzimu woyera amatipatsa mphamvu zimene tifuna kuti tikhale a kristu opambana.



Mu phunzitori tizaona pa mphamvu ili kwa ife kucokera kwa mzimu woyera.

Werengani yohane 20:22

Kodi yesu anacita ciani kwa ophunzira ace?

Kodi ananena ciani kwa iwo?

Mau a cihelene o tanthauza <anawapumira> pano ndi emphusao. Apa ndipo peka pamene aya gwiritsa nchito muchipangano ca tsopano, koma mu cipangano ca kale mu cihelene aya gwiritsa nchito mu Genesis 2:7. Werengani iyi ndime. Ndani anawapumira?

Anapumira ndani?

N'ciani cinacitika?

Pamene Mulungu ana pumira Adamu, Adamu anakhala ndi moyo. Uku ndiko kulengedwa kwa munthu. Motero pamene Yesu anawapumira ophunzira ace inali nchito yo walenga mwatsopano. Pa kutha kwa ici, Yesu anawapasa ophunzira ace cocita, Macitidwe 1:4 ciani?

Kulingana ndi Macitidwe 1:5 lonjezo la atate ndi ciani?

Werengani Macitidwe 2:1-4. Lonjezo la atate lina patsidwa liti?

Papita zaka zikwi ziwiri kucokera pamene kacisi inapatsidwa mzimu woyera. Nchito yathu kwa mzimu woyera isiyana na ija ya ophunzira ace. Anayembekeza kufikira atabwera. Manje sityembekezera cifukwa anabwera kale. Tiyeni tione zimene tiyenera kucita kwa mzimu woyera.

Tiona kucokera mu macitidwe a atumwi pamene uthenga wa bwino unalalikidwa unaitana kavomekedzana kwa onse anthu atatu a umulungu. Kucokera mu ndime idzi, fotokodzani zimene cipangano catsopano cinena pa munthu ndi munthu. Macitidwe 20:21, 2:38, 8:15, 19:2

Yankho yanga kwa atate

Yankho yanga kwa mama

Yankho yanga kwa mzimu woyera

Tiyenera kutembenukila kwa atate, kukhulupilira mwa ambuye yesu kristu ndi ku landira mzimu woyera. Mzimu woyera ndi caulele (onani Luka 11:13, macitidwe 2:38, 8:20, 10:45, 11:17). Zilangizo zonse zili mucipangano ca tsopano zimene zinena pacimene tiyenera kucita kwa caulele ca mzimu woyera zitiuza kumulandira.

Kubatzika ndi mzimu woyera kapena kumulandira, si matero ai, koma ndi ciyambi ca umoyo waku mzimu watsopano.

Ndikulimbikitsa kwotani kwa patsidwa mu 5:18

Aya mau a mu cihelene pano a tanthauza cili kupitiliza kucitika ici ndi kupitiliza <kukhala o zula> kapena kupitiliza ku zulitsidwa thawi zonse.



ZOCITA

Ubatizo wa ku mzimu wu sintha zinthu zinai mu umoyo wathu.

- 1 Umboni wathu kwa dziko. Kodi Yesu ananena kuti ndi ciani cizacitika ngati tazula ndi mzimu woyera mu macitidwe 1:8

- 2 kulambila Mulungu. Zinthu zotani ananena amene ana batizika ku mzimu pa tsiku la Pentecost mu macitidwe 2:11?

Ngati ta batizika ndi mzimu woyera tilandila lilime la tsopano lo lambila mulungu ndi kumupemphera. Ici cioneka kukhala cobvuta maningi pa zinthu zonse za ubatizo wa mzimu woyera mu kacisi matsiku ano, ndi co dabwisa. Ndi cinthu cimodzi codziwilako za mu cipangano ca tsopano. Ndi cimodzi cokha pa za ulele zisanu ndi zinai za mzimu woyera (pamodzi ndi ku matsula mitundu) ziri mu 1 Akorinto 12 zimene si zina gwire nchito mucipangano ca kale. Ndi cifukwa cace mudyekedzi acizonda. Werengani marko 16:16. Kodi ndani anayamba kunena za malulime mu cipangano ca tsopano?

-
- 3 kuti tikwaniritse kudzimangirira kodi Paulo ananena ciani pali iye wakulankhula mau m'lilime mu 1 Akorinto 14:4

Pamene titenga nthawi kulankhula ndi Mulungu mu ma lilime mzimu wathu uzakulilako.

- 4 Utumiki wathu ku kacisi

Kuli zipaso za ulele za ku mzimu zisanu ndi zinai zimene Paulo alemba mu 1 Akorinto 12:4-11. Paso za mzimu woyera ndizo cokera kwa Mulungu. Ndipo zima gwira nchito ngati mzimu woyera upita mu anthu. Colinga cace ndi kuti, mphamvu za Mulungu kupitila mu mau, cibvumbutso, kapena cocitika, kacisi ya Mulungu imangire.

Mukusiliza pa 12 June 1979 mbiri yo yendesa ndeke yinabuka pamene munyamata anayendesa ndeke yo chova ndi miyendo kutauka English Chanel. Uyu ulendo wa makilometer makumi atatu ndi asanu unasila mu ma hours atatu. Ndipo ndeke iyi inambululuka ma meters asanu pa mwamba pamadzi. Munyamata uyu anafika ku sidya la France wo topa.

Tiyamike Mulungu pa ndeke za makina! Tiyamikanso Mulungu pa Mzimu woyera. Asakhale kucokera mphamvu zimene sitigwiritsa nchito.

PHUNZIRO 10 KUYANJANA

Mkazi amene mwamuna wace anafa mwazizizi ndi matenda a mtima anaganiza kuti ana ace awiri asapezeke ku malilo cifukwa anali ang'ono. Anaganiza kuti kuona chitanda ca atate wao cilowa mumanda cingakhale cinthu cowabvuta kwambiri mu umoyo wao cifukwa anali ana ang'ono. Mbeu ya mantha inalowa mu umoyo wa anawo. Anali kumvera mantha nthawi zonse akapita pafupi ndimanda awo.

Tsiku lina mkazi wamasiyeyo anapita ku manda a mwamuna wace ndi mzace, na itana ana ace kuti apite nao. Mwana wumungo'no anavomera kupita naye kumanda, koma wa mkuru ananyalanyaza cifukwa anali ndi mantha kwambiri. Mwana wamung'ono anali mkazi ndipo ana kondwera kwambiri pamene anaona malemba apa mwala wa pa manda onena kuti atate ace anali munthu wa cifundo ndi ulemu.

Mzace wa mkazi wamasiyeyo anaganiza cinthu cimene cinaoneka kukhala cacilendo. “Tsiku lina tikabwere kudyela cakudya pano pamanda,” motero ananena. “Ndikulakwa kuganiza kuti ano ndi malo oganizilapo imfa cabe.” Ananenanso, “Ano ndi malo osangalalilapo mu umoyo ndi kupeza mphamvu za tsopano zo khalilamo mu umoyo wathu,” ananena.

Ici cinthu cosabvuta codyela pamodzi cakudya pa manda ya atate wao cinawapatsa ana awirawo kudziwa kuti panalibe coopya pa imfa ya atate wao. Motero ana gwirisa nchito m'pata uyu ku kumbukira zinthu zabwino zimene tate wao anali kucita.

Nkhani yodyela cakudya pa manda ingaoneke ya cilendo, koma ilingana ndi cimene Yesu anatiuza kucita. Akristu ana cizolowezi cokumbukira mwamene Yesu anafera m'malo mwao kupyolera mu kudya mkate ndi kumwa vinyu. Iyi nthawi yo kumbukira timaica kuti 'kuyanjana.'



Mu phunzitori tizaona cimene buku lo patulika liphunzitsa pa kuyanjana.

Werengani Mateyu 26:26-28

Ndi ciani cimene Yesu ananena ndi kucita mu ndime ya 26?

Ndi ciani cimene ananena ndi kucita mu ndime ya 27 ndi 28?

Onani Yohane 6:47-63

Yesu ananena ciani mu ndime ya 51 ndi 53?

Kodi ayuda ananena ciani pa ici mu ndime ya 52?

Kodi ena mwa ophunzira ace ananena ciani mu ndime 60?

Anayanka ciani mu ndime 66?

Pamene yesu ananena kuti omusatira onse ayenera kudya thupi lace ndi kumwa mwazi wace pakuti akhale ndi moyo wa kuuzimu anali kunenela mu mafanizo. Nthawi zina ananena kuti “ndine citseko,” “Ndine mtengo wa vinyu,” etc. ndi coonekeratu poyera kuti anali kunenera mu mafanizo sanali kufuna kuti amene anali kumvwa akhulupirire kuti ndiye citseko coonadi kapena coonadi ndiye mtengo wa vinyu.

A Yuda ndi ophunzira ace amene ana khumudwitsidwa anasokoneza mu kutanthauza mau a yesu kweni kweni. Ndicofunikira kuti na ife tisalakwenso pa kulandira mugonero, kuganiza kuti mkate wamene timadya ndi zoonadi thupi la yesu, ndi vinyu ndi zoonadi mwazi wace. Ndi zinthu zimene ziimilila thupi ndi mwazi wa Yesu.

Yesu ananena ciani mu ndime 63?

Pamene tilandira mugonero tionetsa cikhulupiriro cathu mwa Yesu, amene anapeleka umoyo wace cifukwa ca ife. Monga mwamene mkate umapasila thupi mphamvu, Yesu amapatsa myoyo zathu mphamvu. Mwachikhulupiro tilandiranso umoyo wace mwatsopano pamene tikudya mkate wa mugonero. Mwazi wace unataika kuti macimo athu a khululukidwe, ndipo tionetsa cikhulupiriro cathu mu cikhululukiro ndi kuyeretsa kwace pamene tikumwa mu cikho ca mugonero.

Lembani izi ndime mu mau anu:

Ndime 54 _____

Ndime 56 _____

Kuli mazina ambiri amene cipangano catsopano cagwiritsa nchito kutanthauza kuyanjana. Ndi mazina otani agwiritsidwa nchito mu ndime izi?

Macitidwe 2:42 _____

Mkate utanthauza thupi la kristu limene lina tyoledwa cifukwa ca ife. Koma tsopano ndife thupi la kristu. Kacisi la Yesu kristu ingakhale ndiyo pwanika muzinduswa nduswa ndi ku gawanika dziko lonse la pansi pano koma ili thupi

limodzi cabe. Mogonero utikumbutsa kuti ndife ogwirizana ndi okhulupirira aku mitundu yonse nthawi zonse (1 Akorinto 10:17)

1 Akorinto 10:16 NKJV

Mau a chihelene amene a tanthauza kuyanjana ndi 'koinonia.' A tanthauza kucita cinthu mwa umodzi ndi ena. Mu kuyanjana tonse titengamo mbali mu phindu la umoyo ndi imfa ya kristu.

Akorinto 10:21

Opembeza mafano ku korinto anali kudya pamodzi ku guwa la ziwanda. Anali kulambila mafano. Mo siana ndi ici, a kristu anadya ku guwa la Ambuye monga anali mu cipangano ndi iye.

1 Akorinto 11:20

Cifukwa kuyanjana kunaikidwa ndi Ambuye, cicedwa kuti “Mugonero wa Ambuye.” Ambuye atiitana kuti tidye mugonero mu kwakumbukira kawiri kawiri kufikira akabwerenso.

Werengani 1 Akorinto 11:26-34.

Paulo anena ciani mu ndime ya 26?

Kulingana ndi ndime ya 27 ticita ciani ngati tadya mugonero kosayenera?

Kudya ndi kumwa kosayenera sikutenga mugonero ndi maganidzo akuti sindine woyenera. Ico ndi mukhalidwe osati colesedwa ai! Kulibe munthu amene ali woyenera kutenga kristu. Koma mwa cisomo cace atilenga kukhala oyenera. Kudya ndi kumwa kosayenera ndi kutenga mbali ku mugonero wa Ambuye kopanda kuganizila thupi la kristu i.e. mwamene timatengela abale ndi alongo mwa kristu.

Atiiza ku cita ciani mukuyamba kwa ndime ya 28?

Kuyanjana ndi nthawi yoziyesa tekha. Kodi tifunika ku khululukira kapena ku khululukidwa ndi wina wace wa mu thupi la kristu? Kodi tifunika kuyanjana ndi mzathu wo khulupirira?

Ngati taziyesa tekha n'ciani ati limbikitsa kucita mu cigawo caciwiri ca ndime ya 28?

Njira patsogolo ndi zigawo za maziko kumi la maphunziro la mu Buku Lopatulika. Mazana amakacisi mu Australia amagwiritsa nchito Buku ili kwa maguru ama kristu atsopano.

Njira patsogolo inena pa nkani izi

- Kuzindikira kuti wa pulumutsidwa
- Ndine yani?
- Kupangidwa watsopano mkati
- Buku lopatulika
- Pemphero
- Kusonkhana
- Kuuzako ena za cikhulupiriro cako
- Ubatizo wa madzi
- Kuyanjana

Ken Legg ndi M'busa wa new Beginnings Christian Church ku Reedy Creek, Gold Coast, Queensland, Australia ndiye anayamba/Msogoleri wa Set Free Ministries.

Set Free

Ministries

Setfree Ministries

P.O. Box 4185

Elanora, Queensland, Australia 4221

Phone: (07)55339091

Mobile: 0407 571 938

Email: setfreemin@ozemail.com.au

www.sma-groups-ministry.com